**NAMBALA YA MAYESO: ____________________________**

# THE CHIMUNGU ZONAL EXAMINATION BOARD 2025

**PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION**

## CHICHEWA

**(100 malikisi)**

**Subject Number: P032**

**Nthawi:2h 15mins**

**1:00 – 3:15Pm**

**Tsiku: 20/02/ 2025**

**Dzinalanu: ___________________________________________________________________**
**(Surname First)**

**Dzina la sukuluyanu: ____________________________________________________________**

## Malangizo

1. **Onetsetsani kuti pepela ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi atatu.**
2. Pepalali lili ndi magawo anayi: **Gawo A, B, C** ndi **D.**
3. Lembani dzina lanu ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba pa tsamba lililose.
4. Lembani nambala yamayeso pa mwamba pa tsamba lililonse.
5. Lembani chimangilizo kapena kalata mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi**D**.
6. Muchitebulo chiri pambalichi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
7. Perekani kwa okuyang'anirani kulemba mayeso (Imvijileta) pepala lonseli nthawi ikakwana.

| FUNSO | Chongani zomwe mwayankha | Munomusalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 – 10 | | | |
| 11 – 15 | | | |
| 16 – 20 | | | |
| 21 – 25 | | | |
| 26 - 30 | | | |
| 31 – 35 | | | |
| 36 – 41 | | | |
| 42 – 45 | | | |

**Turn Over**

@ CHIZEBO 2025

**NAMBALA YA MAYESO: ___________________________**

**GAWO A: (Malikisi 30)**

**Langizo:** Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere **100** koma asabzole **150.**

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu " Tsiku losaiwalika"

   **Mwazina tsatani izi polemba**

   **Ndime yoyamba**
   - Lidali tsiku liti?
   - Komwe mudali patsikulo?

   **Ndime yachiwiri**
   - Zomwe zidachitika patsikulo
   - Momwe mudakhudzidwira ndi zochitikazo
   - Zomwe zidachititsa tsikulo kukhala losaiwalika

   **Ndime yachitatu**
   - Mudaphunzirapo chani patsikulo?

   **KAPENA**

2. Mwasankhidwa kukayamba fomu wani kusukulu ya sekondale. Muli kusukuluko, mulembereni kalata mnzanu amene akuyembekezera kulemba mayeso yomulimbikitsa kuti nayenso asankhidwe. **Mwa zina tsatani izi polemba**

   **Ndime yoyamba**
   - Dzina la sukulu ya sekondale imene mwasankhidwira
   - Tsiku ndi mwezi mudayamba sukulu

   **Ndime yachiwiri**
   - Zomwe mudachita kuti musankhidwe.
   - Zina zomwe mnzanuyo angachite kuti nayenso adzasankhidwe.

   **Ndime yachitatu**
   - Maphunziro achilendo ndi zosangalatsa zomwe mwaona ku sukuluko.

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

**NAMBALA YA MAYESO: ____________________________**

**NAMBALA YA MAYESO: ___________________________**

**GAWO B (Malikisi 20)** **KUMVETSA NKHANI**

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo pamizere ili pansi pa funso lililonse.

## NACHITHIDZI ANONG'ONEZA BONDO

Kudali chakum'mawa wa tsiku loweruka pomwe mnyamata wina dzina lake Chikondi ankaperekeza wokondedwa wake, Nachithidzi kumalo kokwelera basi a Mbongozi. Panthawi imeneyi nkuti misozi tothamanga ndi yotentha ngati madzi ikutsikira m'masaya mwa mnyamatayo. Kumeneku kudali kulira polingalira kuti wachikondi wakeyu amachoka kupita kukagwira ntchito ku Lilongwe.

Basi yomwe adakwera Nachithidzi isadafike, Chikondi ndi wokondedwa wakeyo adali akucheza. Pamenepa Chikondi adamuuza wokondedwa wakeyo kuti chikondi chake sichidzasintha ngakhale atakumana ndi mikwingwirima yotani. Adamuuzanso kuti ndi bwino kuti njoleyo isunge khosi kuti mkanda woyera idzavale mtsogolo. Adamukumbutsanso kuti kunja kuno kwaopsa choncho nkofunika kusamala.

Ngakhale mnyamata adafotokoza zonsezi kudali kungotaya nthawi yake chifukwa kwa njoleyo zimkangotulukira mbali ina yakhutu. Zoona zenizeni zidali zakuti Nachithidzi samkakonda Chikondi chifukwa adali mphemvu mdyera kumthiko, kwakwatuke wachabechabe.

Atayamba ntchito ija, mtimawake udaloza kwanjonda ina yomwe idali yokhupuka. Sipadatenge nthawi yaitali, Nachithidzi adamusiya Chikondi uja ndipo adakwatiwa ndi njodza ija ngakhale idali ndi mkazi wina kale. Makolo a Nachithidzi adayesetsa kumuletsa koma poti mwana akalira nyanga yansatsi msemere imufotere yekha, adangomusiya.

Patapita nthawi Nachithidzi adapezeka kuti ali ndi pathupi. Atapita kusikelo ya amayi oyembekezera kuchipatala, adamuyeza ndipo adamupeza kuti ali ndi kachilombo koyambitsa Edzi ka HIV. Pamenepa adakumbukira malangizo abwezi lake Chikondi koma poti madzi akatayika sawoleka, Iye adalira ndi kunong'oneza bondo.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.**

a. Kodi pakati pa Chikondi ndi Nachithidzi padali ubale wotani?
______________________________________________ (malikisi 1

b. Kodi malo amene adakwerera basi Nachithidzi ankatchedwa chiyani?
______________________________________________ (malikisi 1

c. N'chifukwa chiyani misozi ya Chikondi inkatsikira m'masaya?
______________________________________________ (malikisi 1

d. Chimene Nachithidzi adapitira ku Lilongwe chidali chiyani
______________________________________________ (malikisi 1

e. Kodi Nachithidzi ankafuna mwamuna wotani?
______________________________________________ (malikisi 1

f. N'chifukwa chiyani makolo a Nachithidzi ankamuletsa kukwatiwa ndi njonda ija?

______________________________________________________________________

______________________________________________________________ (malikisi 2

g. Perekani zining'a kuchokera m'nkhaniyi zomwe matanthauzo ake ndi awa:

a. Mkazi wokongola ____________________________________________ (malikisi 1

b. Mavuto ____________________________________________________ (malikisi 1

h. Perekani matanthauzo a mikuluwiko iyi yomwe ikupezeka mnkhaniyi

a. "Madzi akatayika sawoleka"
______________________________________________________________ (malikisi 2

b. "Isunge khosi kuti mkanda woyera idzavale"
______________________________________________________________ (malikisi 2

i. Fotokozani chifukwa chimene Nachithidzi adanong'oneza bondo

______________________________________________________________________

______________________________________________________________ (malikisi 2

j. Kodi matenda a Edzi ngoopsa bwanji?
______________________________________________________________ (malikisi 1

k. Lembani mawu ofanana m'matanthauzo ndi otsatirawa kuchokera m'nkhaniyi?

i. "Pakati" ____________________________________________ (malikisi 1

ii. "Yolemera" ____________________________________________ (malikisi 1

l. Mnkhaniyi muli phunziro lotani?

______________________________________________________________________

______________________________________________________________ (malikisi 2

**GAWO C** (Malikisi 10) Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli

4. a) Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

"Chaka chino ndaganiza mozama. Ndikufuna kuti tonse tibzale mbewu ya makono ya chimanga kuti m'mudzi muno musadzadutsenso galu wakuda."

**Mafunso**

i. Ndimalonje anji amenewa?
______________________________________________________ (malikisi 1

ii. Kodi malonjewa akuyankhulidwa kwa yani?
______________________________________________________ (malikisi 1

iii. Mawu oti "galu wakuda" akutanthauzanji?
______________________________________________________ (malikisi 1

b) Kodi pa msewu nyale yachikasu imatanthauzanji?
______________________________________________________________ (malikisi 1

c) Perekani njira imodzi yotumizira uthenga wamaliro m'mudzi

_______________________________________________ (malikisi 1

5. Pangani ziganizo nzomveka bwino ndi mawu awa:

a. Chifukwa (malikisi 1

_______________________________________________

b. Wochenjera (malikisi 1

_______________________________________________

c. Pa (malikisi 1

_______________________________________________

d. Yankhula (malikisi 1

_______________________________________________

e. Mayo ine! (malikisi 1

_______________________________________________

**GAWO D. (Malikisi 40)**

Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C kapena D) m'mafunso otsatirawa

**Mafunso 6 mpaka 10**. Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

6. Bwerani <u>kuti</u> mudzamve yankho
   A. Mfotokozi C Mlumikizi
   B. Mperekezi D Muonjezi

7. Njovu ndi nyama <u>yayikulu</u> kwambiri.
   A. Mlowam'malo C Dzina
   B. Mneni D Mfotokozi

8. Iye apita <u>kwa</u> achimwene ake mawa
   A. Mvekero C Muonjezi
   B. Mperekezi D Mlumikizi

9. <u>Hehede!</u> Sukulu yathu yapambana mpikisano uja.
   A. Mvekero C Mfuwu
   B. Mneni D Dzina

10. <u>Ganizo</u> lanu lamveka.
    A. Dzina C Mlowam'malo
    B. Mneni D Mfuwu

**Mafunso 11 mpaka 15**. Sankhani magulu a mayina omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mzinganizo zotsatirazi.

11. <u>Kalata</u> yanga ndalandira lero.
    A. Ka -, Ti- C Chi -, Zi-
    B. I -, Zi- D U-, Ma-

12. Nkhwangwa yagwera <u>m'madzi</u>.
    A. Mu -, A- C Chi-, Zi-
    B. Ka -, Ti D Ku-,Pa-, Mu-

13. Maukwati adali kale.
    A. U -, Ma- C Mu-, Mi-
    B. Ka -, Ti- D Mu -, A-

14. <u>Chibwano</u> changa chikupweteka
    A. I -, Zi- C Chi -, Zi-
    B. Li -, Ma- D Mu –, Mi-

15. Iye ali ndi i<u>mpso</u> yotupa
    A. Ku -,Pa-, Mu- C Li -, Ma-
    B. I – Zi- D Ka -, Ti-

**Mafunso 16 mpaka 20.** Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zoyenera za m'kalembedwe m'ziganizo zotsatirazi

16. A. Iye adaphunzira luso losoka mphasa.
    B. Iye adaphunzira luso, losoka mphasa.
    C. Iye adaphunzira luso losoka mphasa.
    D. Iye adaphunzira, luso losoka mphasa!

17. A. "Iwo anati timakonda, kusambira"

B'Iwo anati; Timakonda kusambira.

C. Iwo anati, "Timakonda kusambira."

D. Iwo anati amakonda kusambira.

18. A. N'chifukwa chiyani, ukulira?

B. Nchifukwa chiyani ukulira?

C. N'chifukwa chiyani ukulira?

D. Nchifukwa, chiyani ukulira?

19. A. Ogo! Madzi anga atayika.

B. Ogo madzi anga atayika?

C. Ogo? Madzi anga atayika.

D. Ogo Madzi anga atayika.

20. A. Ine ndimadya mtedza, nthochi mbatata ndi mango

B. Ine ndimadya mtedza, nthochi, mbatata ndi mango

C. Ine ndimadya, mtedza nthochi, mbatata ndi mango

D. Ine ndi madya mtedza nthochi, mbatata ndi mango

**Mafunso 21 mpaka 25**. Sankhani mitundu ya aonjezi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi

21. Mwanayu amaganiza <u>mwachibwana.</u>

A. Wanthawi　　C　Wowerenga

B. Wamalo　　D　Wam'chitidwe

22. Osalowa <u>muno</u>.

A. Wamchitidwe　　C　Wamalo

B. Wamuyeso　　D　Wofunsa

23. <u>Makedzana</u> kudali ana opanda mwano.

A. Wamalo　　C　Wochepetsa

B. Wanthawi　　D　Wowerenga

24. Mwafika <u>bwanji</u> kuno?

A. Wam'chitidwe　　C　Wanthawi

B. Wofunsa　　D　Wamalo

25. Mutu ukundipweteka <u>pang'ono</u>.

A. Wa muyeso　　C　Wanthawi

B. Wofunsa　　D　Wam'chitidwe

**Mafunso 26 mpaka 30.** Sankhani chachimuna cha mayina otsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi

26. <u>Mfumukazi</u> yawo ndi yankhaza.

A. Mkamwini　　C　Atsibweni

B. Ndoda　　D　Mfumu

27. Tapatsidwa <u>nkhunda</u> ziwiri ndi agogo.

A. Chipsolopsolo　　C　Mzambwe

B. Tonde　　D　Tambala

28. Iye adabwera ndi <u>apongozi</u> ake omwe.

A. Akamwini　　C　Atatavyala

B. Abambo　　D　Atsibweni

29. <u>Mdzakazi</u> wanga wabwera.

A. Kapolo　　C　Ndoda

B. Mkamwini　　D　Muna

30. <u>Ntchembere</u> zinachezera kuvina.

A. Ndoda　　C　Nkhuzi

B. Mfumu　　D　Mphulu

**Mafunso 31 mpaka 35.** Sankhani mawu oyenera kutsirizitsa mikuluwiko yotsatirayi.

31. Lero lomwe lidadetsa ___________.

A. Khwangwala　　C　Midzodzo

B. Mnthengu　　D　Mafulufute

32. Walira mvula, walira ____________.

A. Mavuto　　C　Matope

B. Misonzi　　D　Ching'aning'ani

33. Pachedwa ________ pali nyelere.

A. Vumbwe　　C　Kalulu

B. Gologolo　　D　Msalu

34. Okoma atani onga _________.

A. Nkhosa　　C　Mfulu

B. Fungwe D Nsomba

35. Kutola ________ ndi m'mawa.
A. Nkhuni C Nyemba
B. Thonje D Khobwe

**Mafunso 36 mpaka 40.** Sankhani mawu otsutsana m'matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

36. Mwana watsitsimuka atam'dyetsa chakudya.
A. Wakhuta C Wadzimbidwa
B. Wakomoka D Wasangalala

37. Agalu alumana chifukwa cha mnofu.
A. Mphonda C Njala
B. Mwazi D Fupa

38. Nzika za ku Malawi zimalimbikira pa ntchito za chitukuko
A. Anyamata C Ophunzira
B. Atsogoleri D Alendo

39. Iye watsimikiza kuti abwera mawa.
A. Watsindika C Wapeneka
B. Wavomereza D Walengeza

40. Wakuba uja wanjatidwa ndi wa polisi.
A. Wamasulidwa C Watetezedwa
B. Wapulumutsidwaa D Wagamulidwa

**Mafunso 41 mpaka 45.** Sankhani mitundu ya nthambi zosayima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

41. Zoti adapita kusukulu ndi zoona.
A. Yamuonjezi C Ya mfotokozi
B. Ya dzina D Yoyima payokha

42. Amayi adafika titatha kudya.
A. Yamfotokozi C Yadzina
B. Yoyima payokha D Ya muonjezi

43. Ana akusewera apowo ndi akwathu.
A. Yoima payokha C Yamfotokozi
B. Yadzina D Yamuonjezi

44. Abambo agulitsa mbuzi yomwe imativutitsa.
A. Yamfotokozi C Yamuonjezi
B. Yadzina D Yoima payokha

45. Iye akulima pomwe panali khola la ng'ombe
A. Yadzina C Yamfotokozi
B. Yamuonjezi D Yoima payokha

**MAFUNSO ATHERA PANO**